EXAMINATION NO: ______________

# NGABU ZONE

**2024 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE OF EDUCATION MOCK EXAMINATION**

# CHICHEWA

(100 Malikisi)

**Thursday, 29 February** **Time allowed:2h 15 Min**

**1:00 -3:15pm**

**Dzina lanu:** ______________________________________________

(Surname first)

**Dzina la Sukulu yanu:** ______________________________________

## Malangizo

1. Onesetsani kuti pepala ili ndimasamba 9
2. Pepala ili ndilamagawo anayi A,B,C ndi D.
3. Lembani dzina lanu ndi nambala yanu pa tsamba lililonse la pepala
4. Lembani kalata kapena chimangirizo pa tsamba la mizere yomwe yaperekedwa pamapeto pa funso 1.
5. Yankhani Gawo B ndi C pa mizere yomwe yaperekedwa pa funso lililonse
6. Yankhani mafunso a mu gawo D pozunguliza lembo A,B,C kapena D
7. Muchitebulo chomwe chili pa tsamba loyamba onetsani funso lomwe mwayankha.
8. Perekani pepalalanu kwa oyang'anira mayeso mukatha kulemba.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26-30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| | | | |

# GAWO A: (30 MALIKISI)

LANGIZO: Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'musiwa sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu 'masewero a kumudzi kwathu' mwa zina tsatani izi polemba
   **Ndime yoyamba**
   - Dzina la masewero omwe amachitika kumudzi kwanu
   - Komwe masewerowo amachitikira
   - Nyengo yomwe masewerowo machitika

   **Ndime yachiwiri**
   - Zinthu zomwe amagwiritsa ntchito pa masewerowo
   - Kufunika kwa maseweowo
   - Magulu a anthu omwe amachita masewero

   **Ndime yachitatu**
   - Zomwe anthu a kumudzi kwanu akuchita kuti masewewo asaiwalike.

   **KAPENA**

2. Yerekezani kuti mwasankhidwa kukayamba fomu 1 ku Sanga secondary sukulu positi ofesi Bokozi 32 Gogontha koma simupita chifukwa mulibe ndalama zolipilira sukulu. Lembani kalata kwa phungu wa kunyumba ya malamulo wa m'dera lanu yopempha thandizo. Mwa zina.

   **Ndime yoyamba**

   - Cholinga chomwe mwalemba mwalembera kalata
   - Ndime mnyamata kapena mtsikana
   - Muli ndi zaka zingati zakubadwa

   **Ndime yochiwiri**

   - Komwe munkaphunzira
   - Mavuta omwe mumakumana nawo pamaphunziro anu
   - Thandizo lomwe mukufuna

   **Ndime yachitatu**

   - Zomwe mudzachite mukalandira thandizolo
   - Ndipo chisangalaro chanu chidzakhala chotani

_______________________________________________

_______________________________________________

_______________________________________________

_______________________________________________

_______________________________________________

_______________________________________________

_______________________________________________

**GAWO B (MALIKISI 20)**

**KUMVETSA NKHANI**

3. Werengani nkhani yotsatirarayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.

Tsiku la mlandu kudadza chikhamu cha anthu. Ambiri adali ndi chidwi chofuna kumva mmene Gwetsani adzayankhulire pa plandu paja.

Ndaipanji adavala mogometsa pa tsikulo. Bambo kachitsa adaimitsidwa kuti alongosore dandaulo lawo. Adalongosola monga adapanganirana ndi akazi awo kuti Ndaipanji apedze banja mwachangu.

“Akuluakulu a bwalo lino, ine dandaulo langa ndi loti mwana wanga Ndaipanji uyo ali apoyo wapatsidwa pathupi ndi a Gwetsani. Ndili ndi umboni kuti kuima kwa mwana wathu , Gwetsani ndiye akudziwa ndipo ngati kuli kukana aliuze bwalo lino. Ine dandaulo langa ndi lomwelo”. A kachitsa adakhala pansi.

Anthu onse adali maso ga! Pa Gwetsani. Akulu a bwalo adafunsa Gwetsani ngati adabwera ndi abale ake. Abale a Gwetsani adaimilira ndi kuzionetsa kwa a bwalo. Iwo adanena kuti palibe tsiku ndilimodzi lomwe abale ake a Ndaipanji adabwera kudzawatulira mlandu. Adanena kuti zonsezo akuzimwera pa bwalopo.

Akulu abwalo adauza Gwetsani kuti aliuze bwalozoona zake malinga ndi zimene zidanenedwa ndi bamboo kachitsa. Gwetsani adakanitsitsa kwa mtu wa galu zopereka pathupi kwa Ndaipanji. Tsono a bwalo adauza Ndaipnaji kuti afotokoze zomwe akudziwa pa nkhaniyo.

Ndaipanji adaimilira ndipo adayankha “ Ine sindine mtsikana ayi, ndine mtchembere kawirikonse. Choncho ndikuuza mopepetsa bwalo lino kuti makolo anga alakwa. Iwo alakwitsa kumtengera mnyamatayu pa bwalo pano popanda chifukwa”

Anthu onse atamva adadabwa a akachitsa achita manyazi pa bwalopo. Koma poti munthu mafuna populumukira mpata ukapedzeka, iwo adaimilira ndikupitilira kuyankhula “ kodi zovala wavala Ndaipanji mukudziwa kuti amene adamugulira ndi Gwetsani yemweyi? Nanga mufuniranji umboni wina pamenepa”

Atayankhula izi ,Ndaipanji adayankhula motere “ ine ndakhumudwa chifukwa chondiganizira kuti ndinalandira zovalazi monga malipiro a chilakolako choipa ndiganiza kuti atopa nane tsono akusowa pondichotsera pakhomopo” pambuyo pake abwalo adagamula kuti Gwetsani alibe mlandu.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pa funso lililonse.

**MAFUNSO**

a) Kodi ndi ndani adakandaula ku bwalo la milandu

_______________________________________________________________________

1 Malikisi

b) N’chifukwa chiyani kubwalo la mlandu kudadza khamu la anthu?

_______________________________________________________________________

2 Malikisi

c) Kodi bambo Kachitsa adali ndi cholinga chotani pofotokoza mlanduwu monga adachitiramu

_______________________________________________________________________

2 Malikisi

d) N’chifukwa chiyani abale ake a Gwetsani adadodoma nayo nkhaniyi?

_______________________________________________________________________

_______________________________________________________________________2marks

e) Kodi chidamukhumudwitsa Ndaipanji nc'chiyani pa mlandu paja?

_______________________________________________

2 Malikisi

f) Nanga Ndaipanji adasonyeza bwanji kuti alibe chinyengo

_______________________________________________

1 Malikisi

g) N'chifukwa chiyani anthu onse adali wodabwa atayankhula Ndaipanji?

_______________________________________________

2 Malikisi

h) Kodi mawu oti 'kuima' akutankhauzanji mn'khaniyi?

_______________________________________________

_______________________________________________

2 Malikisi

i) Perekani matanthauzo a mawu awa:
   a. Maso ga!

   _______________________________________________

   1 Malikis

   b. Mogometsa _______________________________________________

   1 Malikisi

   c. Ntchembere _______________________________________________

   1 Malikisi

j) Kodi Ndaipanji adali ndi maganizo otani kwa makolo ake aja

_______________________________________________

2 Malikisi

k) Perekani mutu woyenera wa nkhaniyi.

_______________________________________________

2 Malikisi

**GAWO C (10 MALIKISI)**

**Yankhani Mafunso onse mugawoli.**

4. Werengani kunkhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

Anapule:Zikomo! Zikomo!

Asitima : Eee! Tiwaope?

Anapule: Ayi musatiope, Kungoti amnzanga kunyumbaku akwatira mkazi wina. Zimenezi zandidandaulitsa polingalira m'mene kunjaku kwaopsera ndi matenda a Edzi.

**MAFUNSO**

A. i). Kodi ndi malonje anji mwawerengawa?

_______________________________________________

ii). Kodi pamalonjewa a sitima ndi ndani?

_______________________________________________

B. Tchulani njira imodzi yotumidzira uthenga wa maliro kumudzi

______________________________________________________________________

C. Kodi mukamayankhula ndi munthu wamkulu mumayenera kutani?

______________________________________________________________________

D. Kodi getsi lofiira imasonjeza chiyani pamnsewu?

______________________________________________________________________

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu mawu awa;
   i. Khuthala ____________________________________________________________
   ii. Choncho ____________________________________________________________
   iii. Bawo ______________________________________________________________
   iv. Mzindo _____________________________________________________________
   v. Zedi ______________________________________________________________

**GAWO D (40 Malikisi)**

Zungulizani lembo lokhonza (A,B,C Kapena D) mafunso otsatirawa.

Mafunso 6 mpaka 10: sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwao mziganizo zotsatirazi

6. Ndagula fanta chifukwa cha iwe.
   A. Mlowam'malo
   B. Mfotokozi
   C. Mperekezi
   D. Mneni
7. Mwana wosamva amachititsa manyazi makolo
   A. Mfotokozi
   B. Muonjezi
   C. Mneni
   D. Mlumikizi
8. Mayo! Njoka yandiluma.
   A. Dzina
   B. Mfuwu
   C. Mneni
   D. Mfotokozi
9. Anyamatawo si anthu
   A. Mlumikizi
   B. Mvekero
   C. Mneni
   D. Mfuwu
10. Alinafe waba zochepa
   A. Mlowam'malo
   B. Muonjezi
   C. Mperekezi
   D. Mneni

Mafunso 11 mapak 15 : sankhani mitundu ya misintho ya aneni omwe ali ndi mzere kunsi kwao muziganizo zotsatirazi

11. Masula mabataniwo
   A. Wochitirana
   B. Wochititsa
   C. Wochitira
   D. Wotsutsa
12. Mwana wandiphera nkhuku.
   A. Wochitira
   B. Wochitirana
   C. Wochititsitsa
   D. Wochitidwa
13. Vinani bwino mukuthirana fumbi
   A. Wamchibisira
   B. Wochitirana
   C. Wochitisitsa
   D. Womchitira
14. Namwino wamwano uja wamenywa
   A. Wochitirana
   B. Wonyazitsa
   C. wotsutsa
   D. Wochititsitsa
15. Wophunzira wamenyedwa ndi aphunzitsi
   A. Wochititsa
   B. Wochitidwa
   C. Wochititsitsa
   D. Womchitira

Mafunso 16 mpaka 20 : sankhani magulu a mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

16. Anthu ambiri amanyadira <u>chinenero</u> chawo
    A. I-zi
    B. Chi-zi
    C. Ka-ti
    D. Mu-mi
17. Nsomba zili <u>m'madzi</u>
    A. Ku-pa-mu
    B. I-zi
    C. Li-ma
    D. Mu-mi
18. <u>Kalata</u> ndalandira lero
    A. Ka-ti
    B. I-zi
    C. Li-ma
    D. U-ma
19. <u>Kambuzi</u> kaja kathawanso
    A. Li-ma
    B. Mu-mi
    C. I-zi
    D. Ka-ti
20. Tikuyenera kusamalira <u>mitengo</u>
    A. Li-ma
    B. Mu-a
    C. Mu-mi
    D. Chi-zi

Mafunso 21 mpaka 25: sankhani mawu ofanana m'matanthauzo omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

21. Tizipereka <u>magazi</u> kuchipatata
    A. Moyo
    B. Mwazi
    C. Ndalama
    D. Matenda
22. Amayi aphika phala la <u>mtombera</u>
    A. Soya
    B. Mgaiwa
    C. Mitama
    D. Chisunje
23. Joni akudwala <u>mkusani</u>
    A. Chimfine
    B. Malungo
    C. Chifuwa
    D. Chibayo
24. Mwana <u>akubangulayo</u> ndi wandani
    A. Akumwetulira
    B. Akuseka
    C. Akukhuluma
    D. Akudandaula
25. <u>Bira</u> wafera pa msewu
    A. Nkhosa
    B. Galu
    C. Ng'ombe
    D. Nkhuku

Mafunso 26 mpaka 30: sankhani ntchito za li izi mziganizo zotsatirazi

26. Iye a<u>li</u> bwino
    A. Kukhala mvekero
    B. Kukhala tsinde la mneni
    C. Kukhala mgiwirizanitsi
    D. Kukhala mpatikira mtsogolo
27. Tsiku <u>li</u>modzi siliwoza mbewa
    A. Kukhala mgwirizanitsi wamawerengo
    B. Kukhala mneni
    C. Kukhala mperekezi
    D. Kukhala mvekero
28. Nda<u>li</u>gwira thupi la mzungu
    A. Kukhala tsinde la mneni
    B. Kukhala mphatikira mtsogolo
    C. Kukhala mgwirizanitsi wamawerengo
    D. Kukhala mgwirizanitsi wapamthera nkhani
29. Khasu <u>li</u>meneri ndi lathu
    A. Kukhala mperekezi
    B. Kukhala mphatikira mtsogolo woloza dzina
    C. Kukhala mgwirizanitsi wamawerengo
    D. Kukhala pamtherankhani
30. Dziko <u>li</u>mazungulira dzuwa.
    A. Kukhala mgwirizanitsi wamwininkhani
    B. Kukhala mperekezi
    C. Kukhala mgwirizanitsi wapamtherankhani
    D. Kukhala mvekero

Mafunso 31-35 : sankhani mikuluwiko yomwe ikutsutsana m'matanthauzo ndi yomwe mwapatsidwayi

31. Ukayendera mzengo usati asakhwi afumbula

A. Padakafunda padajiwitsa galu
B. Ukayendera ntchire wayendera zones
C. Zenegerezu adalinda kwawukwawu
D. Ichi nchiyani mkulinga muli awiri

32. Kuona maso ankhono mkudekha
A. Zengerezu adalinda kwawukwawu
B. Fodya wako ndi uyo ali pa mphuno
C. Pakafunda padajiwitsa galu
D. Ndapakonda adasiya khonde

33. Msinje wa tinkanena udakathera m'siizi
A. Mawu aakulu Akoma akagonera
B. Bza! Sapita kawiri
C. Njuchi zikachuluka siziika uchi
D. Ali derenkulinga utayenda naye

34. Pamodzimodzi padawoletsa dzungu
A. Okaona Nyanja adakaona ndi njuchi zomwe
B. Mwana wang'ono sakulira dziwe limodzi
C. Ukayenda mtchire wayendera zones
D. Kalikokha nkanyama tili awiri n'tianthu

35. Tsabola wakale sawawa
A. Kalulu adaombola njobvu
B. Munthu amalakwa pa munthu mnzake
C. Tunkanena adakathera msiizi
D. Mwana wamwini ndi gaga saunjika

Mafunso 36 mpaka 40 sankhani mitundu ya nthambi ya ziganizo zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

36. Nkhuku <u>imene ikudwala</u> ndiyanga
A. Yamuonjezi
B. Yadzina
C. Yamfotokozi
D. Yoima payokha

37. Mvula ivuta kubwera <u>chifukwa tadula mitengo yonse</u>
A. Ya dzina
B. Yamfotokozi
C. Yoima payokha
D. Ya muonjezi

38. <u>Zoti Nyanja yathu ikuphwa</u> ndi zoona
A. Ya muonjezi
B. Yoima payokha
C. Yamfotokozi
D. Ya dzina

39. Agogo adafuula <u>pamene adaona njoka</u>
A. Ya muonjezi
B. Yoima payokha
C. Yad zina
D. Ya mfotokozi

40. Chuma <u>chimene wabacho ufa nacho</u>
A. Ya muonjezi
B. Ya dzina
C. Yamfotokozi
D. Yoima payokha

Mafunso 41 mpaka 45: sankhani ntchito za alumikizi mziganizo zotsatirazi

41. Anawa agwira ntchito mwaluso <u>ndi</u> mwamphamvu
A. Kulumikiza mayina
B. Kulumikiza afotokozi
C. Kulumikiza aonjezi
D. Kulumikiza alowam'malo

42. Nyambose adabwera <u>ndipo</u> wapita
A. Kulumikiza aonjezi
B. Kulumikiza aneni
C. Kulumikiza mayina
D. Kulumikiza afotokozi

43. Pempha <u>kuti</u> akugawireko
A. Kutsonjeza zotsatira
B. Kugwirizanitsa
C. Kulumikiza mayina
D. Kulumikiza aonjezi

44. Ugule nsomba <u>osati</u> nyama
A. Kusonyeza zotsatira
B. Kugwirizanitsa
C. Kulekanitsa
D. Kulumikiza a fotokozi

45. Iye sabwera <u>chifukwa</u> akudwala
A. Kutayanitsa
B. Kugwirizanitsa
C. Osonyeza zotsatira
D. Kulumikiza mayina

# <u>MAFUNSO ATHERA PANO.</u>